


UTUMIKI WODZAZA NDI CHIKONDI



Phunziro 9, August 29, 2026

"Pakuti
ndinakulemberani kalata
ija ndili wopsinjika ndi
wowawidwa mtima
kwambiri ndi kutuluka
misozi yambiri, osati
pofuna kukumvetsani
chisoni koma kuti
ndikudziwitseni kuti
ndimakukondani
kwambiri."
(2 Akorinto 2:4, CCL)






Pamene tikufufuza mozama Kalata Yachiwiri ya Paulo kwa Akorinto, tikuona kuti mtumwiyu ali ndi chidwi chachikulu pa ubwino wa mpingo.

Ngakhale kuti kutsatira njira za Mulungu sikunakhalepo kophweka m'dziko lodzala ndi uchimoli, mu zaka za zana loyamba za utumiki, kuvomereza poyera kuti munthu ndi Mkhristu kukanabweretsa mavuto aakulu.

Paulo akukonzekeretsa mpingo kuti ukumane ndi mavuto amenewa, kaya ochokera mkati kapena kunja, ndipo akuphunzitsa anthuwo kukhala thupi limodzi logwirizana mwa chikondi chopanda dyera. Kuchokera pa malangizo amenewa, ifenso masiku ano tingaphunzire kukhala “fungo la moyo lotsogolera ku moyo” (2 Akorinto 2:16).



Chithonhozo cha Mulungu m'masautso



Chihero ndi kutsimikiza mu utumiki



Kuchita zinthu mwanzeru



kukhululukidwa ndi kubwezeretsedwa



Fungo lokoma la Khristu



CHITONTHOZO CHA MULUNGU M'MASAUTSO

"Iye amatithonhoza ife m'mavuto athu onse, kuti ifenso tithe kuthonhoza amene ali pavuto lililonse ndi chithonhozo chimene ife tilandira kwa Mulungu. " (2 Akorinto 1:4)

Kalata Yachiwiri ya Akorinto ndi kalata imene Paulo amalankhula kwambiri za chithonhozo. Mpingo unali kudutsa m'nthawi yovuta, ndipo kalata ya Paulo yapita ija inawapangitsa kukhala achisoni kwambiri.

Koma chisoni chimenecho chinali "cha Umulungu," chimene chinawatsogolera ku kulapa (2 Akorinto 7:10). Choncho, Paulo sanafune kuti chisonicho chiwalemsetse kwambiri, koma kuti atonhozedwe.



Iye mwini anadutsapo m'nthawi imene moyo wake unali pachiswe ndipo anataya mtima (2 Akorinto 1:8-10). Koma Mulungu anamuthonhoza, ndipo tsopano akupereka chithonhozo chimenecho ku mpingo (2 Akorinto 1:6).

CHITONTHOZO CHA MULUNGU

Chimatimasula ku mantha

Chimatikumbutsa nthawi zomwe Iye anatithandiza

Chimatithandiza kupirira masautso

Chimatitsogolera ku kukhwima muzimu

Chimatilimbikitsa kupempherera ena.

Timatonthozana monga momwe Mulungu anathonhozera ife

CHIYERO NDI KUTSIMIKIZIKA MU UTUMIKI


“Tsono chonyadira chathu n’chakuti, chikumbumtima chathu chimatitsimikizira kuti timakhala bwino m’dziko lapansi, makamaka pa ubale wathu ndi inu. Takhala moona mtima ndi oyera mtima. Sitinachite chomwechi mwa nzeru ya dziko lapansi koma monga mwa chisomo cha Mulungu.” (2 Akorinto 1:12 CCL)

Anthu ena ankamunyoza Paulo, ankamunene kuti anali wofooka komanso wosakhazikika pa maganizo ake (2 Akorinto 10:10). Pa chifukwa chimenechi, komanso kuti uphungu wake ulandiridwe ndi kuvomerezedwa, zinali zofunika kuti mtumwiyo adziteze ku zoneneza zoterezi.


Monga munthu, iye anadziona ngati wosafunika kwenikweni (Aefeso 3:8). Koma, chifukwa cha chisomo cha Mulungu, anatha kunena modzitamandira kuti anali ndi chikumbumtima choyera (2 Akorinto 1:12).



Iye pamodzi ndi anzake akanatha kunena molimba mtima kuti khalidwe lawo linali loyera ndi loona mtima, mu mpingo komanso kunja kwa mpingo.



Pachifukwa chimenechi, zolembe za Paulo zinalibe zolinga zobisika. Iye ankayembekezera kuti makalatawa aziwerengedwa ndi kumvedwa podziwa kuti analembedwa ndi mtima woyera ndi woona—kutanthauza kuti analembedwa chifukwa cha chikondi pa iwo komanso pofuna kuwapindulitsa (2 Akorinto 1:13-14).



KUCHITA ZINTHU MWANZERU

"Mulungu ndi mboni yanga kuti sindinabwererenso ku Korinto kuno kuti ndisakumvetseni chisoni." (2 Akorinto 1:23 CCL)

Mukalata yake yoyamba, Paulo anauza Akorinto za njira imene anakonza kuti adzadutse (1 Akorinto 16:5-11):

Efeso

Masedonia

Akorinto

Yudeya

Mukalata ina imene analemba pambuyo pake (imene inatayika, 2 Akorinto 7:8), anawauza kuti adzawachezera kawiri (2 Akorinto 1:15-16):

Efeso

Akorinto

Masedonia

Akorinto

Yudeya

Komabe, iye anasintha zolinga zake ndipo adaganiza zoti apange ulendo woyamba umenewo (2 Akorinto 1:23). Kusintha kumeneku kunachititsa ena kumudzudzula kuti anali wosakhazikika komanso wosintha maganizo pafupipafupi. Ndichifukwa chiyani anasintha maganizo ake?

Zinkaoneka kuti kunali kofunika kuti Paulo apite ku Korinto chifukwa cha mavuto amene analipo. Koma kutsutsidwa kumene akanakumana nako kukanayambitsa mkangano umene ankafuna kuupewa, chifukwa cha chikondi chachikulu chimene anali nacho pa iwo (2 Akorinto 2:1-4).




KUKHULULUKIDWA NDI KUBWEZERETSEDWA

"Aliyense amene mumukhululukire, inenso ndimukhululukira. Ndipo ndikakhululukira, ngati pali kanthu koti ndikhululukire, ndiye kuti ndakhululuka chifukwa cha inu pamaso pa Khristu," (2 Akorinto 2:10)

Pamene Paulo anali paulendo wopita ku Troas, Tito anapita ku Korinto. Kuchokera ku Troas, Paulo anapita ku Masedonia. Koma anali ndi nkhwana kwambiri chifukwa chakuti Tito sanakumane naye ku Troas kuti amupatse uthenga wokhudza mpingo wa ku Korinto (2 Akorinto 2:12-13).

Patangopita nthawi yochepa, Tito anakumana ndi Paulo ku Masedonia. Anamuuza mmene mpingo unalandirira bwino kwambiri malangizo ndi machenjezo a mtumwiyu (2 Akorinto 7:5-9, 13-16).



Imodzi mwa nkhani zimene ankafunika kuthetsa inali yokhudza chilango cha mu mpingo. Pomvera mtumwiyu, munthu amene analakwa anadzudzulidwa, ndipo anavomera kudzudzulidwako. Tsopano Paulo akuwapempha kuti achite chinthu chotsatira: kumukhululukira ndi kumulandiranso mu mpingo (2 Akorinto 2:5-11)

KUNUNKHIRA KWA KHRISTU

"Pakuti kwa Mulungu ndife fungo labwino la Khristu pakati pa iwo amene akupulumutsidwa ndi amene akuwonongeka. "

(2 Akorinto 2:15)



Pofotokoza mmene Mulungu "anatsegulira khomo" kuti uthenga wabwino ulalikidwe bwino ku Troa, Paulo akufuula mawu a chiyamiko ndi chigonjetso kuti: "Koma ayamikike Mulungu, amene nthawi zonse amatitsogolera monga akapolo mu ulendo wachigonjetso wa Khristu, ndipo amatigwiritsa ntchito kufalitsa ponseponse fungo lokoma la kumudziwa lye" (2 Akorinto 2:14).

Monga fungo limene limafalikira paliponse, chidziwitso cha Khristu chimafikira munthu aliyense. Kwa Akorinto, monganso kwa ife, fungo limeneli ndi la moyo wosatha. Koma kwa iwo amene amakana kuitana kwa Mulungu, ndi fungo la imfa (2 Akorinto 2:15-16).



Poganizira za udindo umene zimenezi zikubweretsa, Paulo akufotokoza kuti uthengawo uyenera kuperekedwa moona mtima, popanda kufuna phindu lililonse la munthu mwini, koma chipulumutso cha cha omvera(2 Akorinto 2:17).



“Mtumiki wokhulupirikayu anabweretsa uthenga wosangalatsa wakuti kusintha kodabwitsa kunachitika pakati pa okhulupirira a ku Korinto. Ambiri anavomera malangizo amene anali mu kalata ya Paulo ndipo analapa machimo awo. Miyoyo yawo sinalinso yochititsa kuti Chikhristu chitonzedwe, koma inali ndi chikoka champhamvu cholimbikitsa kukhala ndi moyo weniweni wopembedza Mulungu. [...]

Kulapa kumene kumabwera chifukwa cha mphamvu ya chisomo cha Mulungu pa mtima kumatsogolera munthu kuvomereza ndi kusiya tchimo. Izi ndizo zipatso zimene mtumwiyu ananena kuti zinaoneka m'miyoyo ya okhulupirira a ku Korinto.”

EGW (The Acts of the Apostles, pp. 324)